


KUDZA KWACHIWIRI

KWA AMBUYE

 “Zaka chikwi,” zikutikumbutsa zimene zinachitika zaka zapitazo pamene tinakumana pano pa Kachisi, chitsitsimutso chofalikira ku dziko lapansi chisanayambe. Ndipo, Atate, Mulungu, ife tikunyadira maganizo amenewo. Ndipo pakupezeka tiri abwinobe mmiyoyo yathu tabwereranso usiku uno kudzayamba misonkhano ya chitsitsimutso yachikale pamene ochimwa amakhoza kupempha chifundo, ndi akugwa amakonzanso moyo wao kwa Mulungu. Ndipo Mzimu Woyera ndiye Munthu wopambana mu msonkhano, Amene amakhuza nalamulira, ndi kutibweretsera Mkate wa Moyo kupyolera mu Mawu. Ndipo ife tikupemphera kuti Iye adzatumikire kwa ife pakutha pa chitsitsimutso cha usikuwu, pochiza odwala ndi osawa, kuyeretsa okhulupirira aliyense, nalandira ulemerero pa kudzipereka kwathu konse komwe tikuyikapo. Pakuti, Atate, Mulungu izi tikuzipempha pongofuna kupereka ulemu ndi ulemerero kwa Dzina Lake. Amen.

² Uku ndi kukwaniritsa kwa lonjezo limene ndinalipanga zaka khumi ndi chimodzi zapitazo. Patenga nthawi kuti ndikwaniritse, kudzanso ku Kachisiyu kudzachita chitsitsimutso. Ndipo, tsopano, ife tikudziwa kuti Kakachisi kathuka kalibe malo okwanira kuchitiramo chitsitsimutso, koma tidzangopanikizanso, mwa njira iriyonse momwe tingathere, kwa usiku ungapo ukudzawu, mwa ulemerero kwa Mulungu.

³ Ndipo ndimakonda kukhala ndi msonkhano mu tchalitchi. Ku malo ambiri, timachitira pa mabwalo amasewero, ndi panja kumakwalala, ndi ku malo ochitirako zoyipa, koma pali kusiyana kwina pamene muchitira mu tchalitchi. Kumaoneka kuti kumakhala chiyanjano chokomerapo, chapafupiko pamene mukhala mu tchalitchi. Uko ku malo a zoyipa, zinthu za chikunja, timangothokoza chifukwa cha mwayi wokumanirako, koma kumangokhala ngati umamva kupsyinjika, monga mphamvu ya ziwanda, zimene umayenera kuziphwasula chitsitsimutso chisanayambe. Ndipono ukadza ku tchalitchi, amakhala malo amene Mulungu amakhalako, ndiko kudza ku nyumba Yake kudzasonkhana.

⁴ Ndipo tsopano ife tikukondwera usiku uno pakuona nkhope zakale zambiri zimene ndinazona zaka zapitazo pa kutsiriza kwa utumiki wanga pa Kachisi pano. Kuona M’bale Graham ali muno, ndi M’bale Curtis ndi Mlongo Angie, ndi Mlongo Gertie

kuno, ndi M'bale Cox ndi Mlongo Cox, ndi, o, mai, ambiri a inu, Mlongo Spencer ndi M'bale Spencer, ndi onse inu muno. Tiri okondwa kwambiri. Mama, ndi Akazi a Slaughter, ndi m'bale uyu apa, gulu lopambana lanuli, mpaka lero. Ndi angati amene akhala ali muno kuyambira pa nthawi imene tinkayamba ija, ndikutanthawuza pamene ndinachoka mwa chitsitsimutso kupita kunja? Titaona manja anu. Mu tchalitchi monse usiku uno, tangoonani manja. Ndi zabwino zedi.

⁵ Tsopano ife tiri. . . kudziwa kuti zitsitsimutso zimadza ndi Mzimu Woyera wokha. Iye ndiye M'modzi Amene amabweretsa chitsitsimutso. Ndipo ife sitingathe mwa ife tokha; ife tikhoza kungosonyeza kulimbikira kwathuko; ndipo Mulungu ayenera kudalitsa kulimbikira kwathuko, ndipo ife timadalira kuti Iye atero.

⁶ Ine ndinali kuuza mkazi wanga pa msewu. . . Ndinalibe ngakhale mwayi wakuti ndidye chakudya cha madzulo lero. Ndi kutanganidwa kwakukulu. Inali 2 koloko dzulo madzulo ndisanavale ngakhale malaya nkomwe, kuchokera pa nthawi imene ndinadzuka dzulo mmawa. Imeneyo ndiyo mbali ya telefoni. Ndipo inali itangokwana 2 koloko pamene ndinayitanidwa mwansanga ndi a Dokotala Sam Adair mu Louisville. Ndipo pamene. . . Ndipo kenako kuyitanidwa kwina kwambiri, ndi achikulire. M'modzi wa ku chipatala, anati, "Koma ife tayembekezera nthawi yaitali, ndipo sitikudziwa ngati gehena ali woipa koposa kuzunzika kumene takhala nako, pakudikira." Ndipo kwangokhala kufuula ndi kulira kochokera kulikonse, mazana a alaliki.

⁷ Ndipo, ndikukuuzani, tikukhala mu masiku opambana ena onse analipo mdzikoli, imodzi mwa nthawi zopambana. Ndipo ndiri wokondwera pakuona njala mu mitima ya anthu yakufuna Mulungu kwambiri.

⁸ Tsopano chiri pa mtima wanga, kupempherera kuti zikhale mwa chifuniro cha Mulungu. Ndipo, pajatu, pali anthu ena amene angoyima kumbuyoko. Ine ndikudabwa. . . Tiri ndi—mpando pano, malo okhoza kukhalapo, ndikudabwa ngati sikungatheke kukonza mpando uwo. Ena mwa madona. . . kapena ena; amene ayima kumbuyoko, kuti mwina tikana. . . Kuno, ndikudabwa ngati awa ali kunowa kapena ena sangangoyenda ndikudzakhala pa mpandowa, kuno kutsogolo. Mwina. . . M'bale Ben, takondwera kukuonani, nthawi yomwe ndinatsirizira kukuonani inu kunali ku San Fernando Valley, California, masabata angapo apitawo. Ndipo pano pali malo ngati mungawone kofunika kudza, inu—abwenzi amene mwayima kumbuyoko. Ndipo tsopano, ngati mukufuna kudza teronino. Pano pali mpando wapadera ku guwa kuno, ndi madanga enanso kuno, ndipo ayenera kukhalidwa ku guwa kuno. Tikufuna inu mukhale motakasuka momwe mungathere.

⁹ Ndipo ndinamuza mkazi wanga kuti ndinadzilonjeza ndekha kuti mwa kuthandiza kwa Mulungu, sindikulinga zolalikira nthawi yaitali, ndikufuna kungolankhula maminiti 30, Ambuye akalola. Ndipo zikhala zozizwitsa ngati nditi ndithe kutero, chifukwa ine—sindimatha kungoyambiratu mofulumira. Ndipo koma ine—ndingoyesa, chifukwa cha . . . Ndipo nthawi imene ikudza tidza, izi, mawa usiku . . .

Usiku uno, phunziro langa ndi: *Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye.*

¹⁰ Ndipo mawa tidzakhala ndi usiku wa mgonero, ndipo ndikufuna kudzalankhula za *Mgonero* kuchokera ku Chipangano Chakale momwe zinaliri. Ndipo ife tiri . . . Usiku wa mawa ndi usiku wa mgonero movomerezeka konsekonse, pakuti ndi usiku umene Ambuye anaperekedwa. Ndipo ndi usiku wovomerezeka wa mgonero. Ndipo tikadzatsiriza ulaliki wathu usiku uno, ulaliki wa monga tichita nthawi zonse, ndiyeno tidzakhala ndi mgonero. Ndipo aliyense akuyitanidwa kudza nafe ndi—nadzanyema nafe chakudya chaulemelo ichi chimene Ambuye Yesu wathu anatisiyira.

¹¹ Ndipono usiku winawo, Ambuye akalola, pokhala usiku wa kupachikidwa, ndikufuna ku—kudzatenga, mwa njira ina uthenga womwe muti mudzaumvere pa mawailesi, wa *Kupachikidwa.*

Ndiyeno usiku wa Loweruka, *Kuyikidwa M'manda.*

¹² M'mawa wa Lamulungu nthawi ya 6 koloko, msonkhano wa pakutuluka kwa dzuwa. Nthawi ya 10 koloko, msonkhano wa ubatizo, ngati pali iwo amene akufuna kubatizidwa. Kenakono uthenga wa mmawa wa Chiukitsiro.

¹³ Ndipo usiku wa Lamulungu, Ambuye akalola, tikuyembezera kudzakhala ndi uthenga waufupi wa *Umboni wa Chiukitsiro*, ndi ulaliki wa machiritso. Maulaliki a machiritso monga momwe timakhala nayo pa msonkhano uliwonse—msonkhano wa momwe tichitira nthawi zonse, udzakhala usiku wa Lamulungu likudzali. Ndipo ngati simunaonere, kapena anzanu sanaone umboni wooneka ndi maso wa Yesu woukitsidwayo, ine ndikuyembekeza kuti Iye adzachita zomwe ankachita zaka zapitazo mu misonkhano, kuwonekera pomwe pano nachita zinthu zomwezo zimene Iye ankachita pamene anali pa dziko lapansi. Ndipo tikuyembekezera nthawi imeneyo, kudza . . . imene ikudza.

¹⁴ Choncho ndiye bwino, yandikirani konkuno ndi kukhazikika motakasuka momwe mungachitire. Ndipo ndikudabwa mwina usiku wa mawa ngati titadzakatenga mipando ina kwina kwake. Mwina uko ku—ku malo osonkhanira maliro kapena kwina kumene tingakapeze yina yowonjezera, mwina kuti tidzangoyiika mozungulitsa m'mbalimu. Tikufuna aliyense akhale motakasuka monga momwe angathere.

15 Ndi angati amene mukukonda Ambuye ndi zonse zimene ziri mwa inu? Tsopano tiyeni tikhazikitse kukhumba kwathu kwa Khristu ndi kungoyang'anitsitsa tsopano. Ife sitinadzere pano ziphunzitso, koma tadzera kudzapembedza Ambuye. Ndipo ife tikungoyitana aliyense wa chiphunzitso, mtundu, khalidwe lirilonse, ziribe kanthu pano, tikungobwera kudzapembedza Ambuye, ndipo padzakhala theka la ora la kuyimba kwachikale ndi—ndi msonkhano usanayambike. Ndipono, mawa usiku ndidzayesa kuyamba monga momwe ndachitira usiku uno, chimodzimidzi, ngati kutheka, nthawi ya 8 koloko, ndi kuti tidzatuluke nsanga momwe tingathere kuti tikakhoze kudzanso usiku winawo.

16 Ndipo, tsopano, aliyense ali wolandiridwa. Ndipo, alendo athu, inu mudzalandiridwa koposa kudza ku chiyanjano chathu ndipo msonkhano utangotha, inu anthu a mpingo uno amene mumasonkhana muno, muonetsetse kuti mugwirane chanza ndi wina aliyense amene mungathe. Mungo... Ingomasukani tsopano, ndi kukhala ndi nthawi yabwino. Ndipo inu simukudziwa chimene Ambuye angachite, ino ndi nthawi ya Chiukitsiro ndipo tikungoyembekezera zinthu zopambana.

17 Tsopano, mu Mawu odalitsika, ndikufuna kungowerenga ndi—ndime kapena mzere umodzi kapena iwiri, kuchokera mu Uthenga Wabwino wa Luka Woyera, ndipo pa mutu wa 15 ndime ya 8:

“Kapena ndi mkazi wotani amene angakhale ali ndi zigwinjiri khumi za siliva, ngati atati wataya chigwinjiri chimodzi, amene sayatsa nyale nasesa m'nyumba, nafunitsitsa mpakana atachipeza?”

Ndipo pamene achipeza, iye ayitana abwenzi ake ndi anthu apafupi naye, nati, Sangalalani nane; pakuti ndapeza chigwinjiri chimene chinanditayika.

18 Tsopano, limenelo likhoza kumveka ngati Lembo losagwirizana ndi za Kudza Kwachiwiri Kwa Khristu, ndi... koma likukamba za Kudza Kwachiwiri kwa Khristu. Ndipo phunziro lalikululi limene tiri nalo patsogolo pathu tsopano ndi limodzi mwa maphunzitso ofunika mu Malembo Oyera onse. Palibe china chopambana monga Kudza Kwa Ambuye Yesu. Pakuti ngati lye sabwera, ife ndiye tapezeka kuti tiri mboni zonyenga; akufa athu amene ali m'manda atayika, ndipo palibe chiyembekezo chinanso chotsalira kwa ife ngati Yesu sadzadza mowonekanso ndi maso kachiwiri. Ndipo momwemo... kuwala uku, mkuwala komweko kwa Kudza Kwachiwiri, kunali kofunika, mwa kuti sabata lopatulika limene tikuyandikirali, limene Yesu, pamene anali kulifika pa nthawi yoyambayo mu mthunzi weniweni wa Mtanda, Iye analankhula pang'ono za imfa Yake, kuyikidwa m'manda ndi chiukitsiro. Iye analankhula kwambiri pa za Kudza Kwake Kwachiwiri koposa momwe

analankhulira pa za imfa, kuyikidwa m'manda, ndi chiukitsiro Chake. Kotero m'kuwala kwa izi, liyenera kukhala phunziro lofunika kwambiri.

¹⁹ Mu Chipangano Chakale, muli nthawi zochuluka Malembo ambiri mu Chipangano Chakale okhuza za Kudza Kwachiwiri Kwa Khristu kuposa zomwe ziripo za kudza koyamba kwa Khristu. Chirichonse kwa mtundu wa anthu, tsopano chitatha kuchitidwa chitetezero, tikudalira kwathunthu pa Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye.

²⁰ Tsopano, tiri ndi zipembedzo zosiyana, ndi zolinga zosiyana, ndi nzeru za masukulu aubusa zambiri, koma chipembedzo chatu cha Chikhristu chinakhazikitsidwa kwenikweni pa kufa, kuyikidwa m'manda, ndi chiukitsiro, ndi Kudza Kwachiwiri kwa Ambuye. O, ndi funso lopambana. Ndipo pamene tikuyandikirano, mwa kulingalira kwanga kowona konse, ife tikukhala mu mthunzi wa Kudza Kwake Kwachiwiri. Pamene, kuona kwanga mwa kuwala kwa Malembo, palibe chiyembekezero china chimene chatsalira kwa Mpingo kupatula Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye. Dziko momwe lakhalira mu chisokonezeko chake lafika kwathunthu posakhozanso kulisamalira, ngakhaleonso mabungwe onse opangidwa ndi anthu a mu dziko. Mafumu sakuthanso kuwalamulira owatsata awo, ngakhale olamulira ndi ukali omwe sakutha kuwopyeza mokwananso, Boma la demokarase silikuwagwiranso anthu moyenera, ndipo palibe chiyembekezo chimene chatsala koma Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye Yesu basi.

²¹ Ndipo tsopano ndi nthawi yina yowopsya kwambiri kwa osakhulupirira ndi ochimwa, imene sanayione konse, chifukwa nthawi ya chiwonongeko ili pafupi. Ndipo ndi nthawi yodala koposa kwa wokhulupirira, pakuti chiwombolo chake chiri pafupi. Pali magulu awiri pa dziko lapansi usiku uno, okhulupirira ndi osakhulupirira. Amene Ambuye akudza kudzawatenga, ndi amene Ambuye akudza kudzawaononga. Pa Kudza Kwake, adzadalitsa mmodzi natemberera wina, pa kuonekera Kwake.

²² Ndipo pokhala kuti ichi ndi chinthu chofunika chotere, ine ndikuganiza kuti lisana... madzulo, kani, pa kachitsitsimutso kathuka, kuti tiyang'anitsitse pa Malembo, ndi kuona kuyandikira kwathu momwe tiriri. Ndikadafuna kudziwa nthawi pakali pano, ndikadayang'ana pa wotchi yanga. Ndikadafuna kudziwa tsiku la pa sabata lomwe tikukhalamo, kapena mwezi wa chaka, ndikadakayang'ana pa kalendala. Ndipo ngati ndikufuna kudziwa kuyandikira kwa nthawi ya chinthu chopambanachi, ndiyang'ana pa Mawu a Mulungu, Iwo amandiuza za nthawi yomwe ichi chiri pafupi. Pakuti Baibulo linati, "Pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika, tukulani mitu yanu, chiwombolo chanu chiri pafupi." Nthawi yayandikira.

23 Chinali chinthu chopambana kwa Yohane mvumbulutsi, pa Chisumbu cha Patmo, pamene anawona chionetsero cha Kudza Kwa Ambuye. Pamene iye anawona matemberero amene anayikidwa pa osakhulupirira, ndi madalitso amene anayikidwa pa okhulupirira, anafuula kuti, “Ngakhale ziri choncho, idzani Ambuye Yesu!” Zinadolola mtima wake atatha kuwona zonse, zochitika Ambuye Asanadze, nafuula “Ngakhale ziri choncho, idzani Ambuye Yesu!” Ndipo pamene m’badwo wonse wa mpingo unatha kupyola pamaso pake, ndipo iye anawona zazikulu zonse, mwa njira yomwe zidzachitikira, ndiye anafuula, “Idzani, Ambuye Yesu!” Chiyenera kukhala chinthu cha ulemerero kudziwa kuti Kudza Kwa Ambuye kuli pafupi.

24 Yesu, pamene ophunzira Ake anafika pa malo aja oti ankayang’ana zinthu za chithupithupi kapena zinthu zolengedwa za pa dziko lapansi. Tsopano, apa tikufuna kuyimapo maminiti angapo. Sizienera kumangokhala za chithupithupi zokha zimene zingatikoke; nthawi zina zinthu za chithupithupi chabe zimatikoka. Atumiki a Yesu kapena ophunzira Ake, ankamulozera Iye kachisi wa mzindawo, Yerusalemu, Kachisi wotchuka pamene Mulungu mwa Ulemerero Wake wa Shekinah anawonekera ku Chipinda Choyeretsetsa. Ndipo pamene anali kumuuza Iye momwe miyala inasanjikizidwira bwino, momwe ukatswiri wopambana wa Mulungu unakonzeratu kuti miyala iyi yomwe inakadulidwa ku malo osiyana a mdziko lapansi niyibweretsedwa pamodzi. Kutu, mwa zaka 40 za kumanga kwake, panalibe ngakhale kumveka kwa macheka kapena kumveka kwa nyundo. Zinangoyikidwa pamodzi mwa ukatswiri. Ndi momwe Mulungu anadzera pakati pa Akerubi ndipo chinaonetsera Ulemerero Wake wa Shekinah, ndi momwe analiri ndi chiyembekezero chachikulu pa kachisi wotchukayu.

25 Ndipo Yesu anawauza iwo, “Musaone zinthu zonsezi.” Komatu anali malo opatulika, anali malo abwino. Anali malo, nyumba yokhalamo Ambuye. Koma Yesu anati, “Musaone zinthu zonsezi. Ine ndiri ndi china chofuna kukuuzani inu chimene chiri choposa izi. Pakuti nthawi ikudza.” Iye anati, “imene sipadzakhala mwala umodzi pa unzake.”

26 Ngakhale tiyese kusamalira matupi athu motani, ngakhale tirimbikire ntchito ya bungwe lathu chotani, kugwira ntchito molimbika mu mpingo pa zathu—madongosolo athu a mpingo, ikudza nthawi pamene zinthu zonsezo zidzathawa ndi kutha.

27 Yesu anayamba kuwauza iwo zimenezo, ndipo iwo anati, “Chizindikiro cha kudza kwa chitsiriziro cha dziko ndi chiyani?”

28 Ndipo anayamba kulankhula nawo kuti, “Nthawi idzafika pamene sipadzakhala mwala umodzi pa unzake. Mudzamva

za nkhondo ndi mbiri za nkhondo, mliri, zivomezi mu malo osiyanasiyana.”

²⁹ Ndipo tsiku lina, ku California, uko ku Oakland, pamene unali mwayi wathu wokhala nawo kumeneko pa msonkhano, ndipo kanali koyamba kuti mkazi wanga akakhale pa malo chivomezi chikuchitika. Ine ndinali nditakhala mu nyumba yometetsera, ndipo ine . . . chipinda chinangogwedeze pang’ono. Ndipo waillesi inalengeza mofulumira kuti, “Chivomezi chagundika.” Nati, “Akuyembekezera china pasanathe maminiti asanu ndi atatu.”

Ndipo ine ndinaganiza, “O, nanga chimenechi chitakhala chotsiriza!”

³⁰ Ine ndinafulumira kuchokera ku nyumba ya ometetsa, ndinakomana ndi mkazi wanga amene anali kundiyembekezera pa msewu, tinakalowa mu sitolo kuti tikagule makadi okhala ndi zithunzi kuti tiwatumizire okondedwa athu. Ndipo tiri komweko, ndinangomva m’thupi mwanga kudabwitsa koseketsa kumene munthu wina aliyense akhoza kumwa, dziko lonse linangoyamba kuvina. Mabotolo anayamba kugwa kuchokera pa alumali, zogumuka zinayamba kugwa kuchokera pa manyumba, nizigwera mu msewu, kumagubuduzika, anthu akufuula ndi kulira pamene pulasitala wa nyumba amagwa kuchokera pa makoma. Ndipo nyumba zazikulu zosanjikizana zipinda 30 kapena 40 kupita m’mwamba, zinavinavina palimodzi mpakana pomwe utsi ndi fumbi lochokera mu dothi lomangira nyumbazo linakwera m’mwamba monga chibowa chachikulu. Ndipo anthu anayamba kufuula nathamanga. Ine ndinati, “Chimenecho ndi chala cha Mulungu Wamphamvu ’chikuti ‘Chilembo chiri pa khoma!’”

³¹ Yesu anati, “Pamene mudzamva za zivomezezi ku malo osiyanasiyana.” Dziko linang’ambika pa misewu yayikulu kwa mtunda wautali, pafupi mapazi asanu, ndipo mng’aluwo unalowa, pansu mwa kuya kwa mapazi mazana. Malo ena, msewu wonse unagumukira. Ndipo ndinaganizira pamene mng’alu umenewo unalikutseguka, kuti ndimakhoza pafupifupi kuona chala cha Mulungu Wamphamvu akuti, “Ndipo kudzakhala zivomezi mmalo osiyanasiyana.”

³² Pamene tsiku linali kupitirira, zivomezezi zisanu ndi zitatatu zinagwedeza mzindawo. Ndipo nyumba za mowa zinali chitsegulire, ndi anthu oledzera mowa anali piringupiringu mmisewu. Ndipo azimayi anali akuyenda mmisewu, atavala mwa pafupi kuvula, ndi zina zonse kungokhala ngati panalibe chimene chimachitika. Anthu masiku ano akhazikika pa dziko lapansi mpaka kuti ine sindikudziwa chimene chingachitike kuti dziko ili ligwedezeke. Anthu akungowoneka ngati sizikuwakhuza. Iwo sakusamala. Ndipo bambo wina anakhoza kuchitira ndemanga, pamene ndinamumva ndi kumuwona ndi

maso anga nati, “Unawona chimene ndinachita? Ndinagwedeza bagera langa. Ine ndi mwamuna wamphamvu.”

Ndipo ndinaganiza, “Kunyoza kotero!”

³³ Sindinkadziwa kuti umenewo ndi mwano mpakana pamene mu mzinda wathu uno, pa msewu madzulo ndikupita ku Georgetown, apa pamene timadutsa usanafike ku msewu waukulu watsopano. Panali chikwangwani chachikulu pamene, chomwe chimati “Iye wauka, Ali ndi Moyo.” Ndipo chikwangwani china utangopitirira ichi, zinali ziwiri zokhazi, chimati, “Kumene kuli mowa wa Budweiser, kuli moyo.”

³⁴ Ine ndinaganizira kuti, “Akuchitiraji mwano wotero!” Ndi chimene akuchita pamene. Baibulo linatinso choncho kuti, “Kudza Kwachiwiri Kwa Khristu kusanachitike, anthu adzakhala amwano, oyenda mu njira za kukhumbira kosakhala kwa umulungu, odzitama ndi onyoza amene ali abwino.” Dziko momwe lafikira mu chinyengo chotere!

³⁵ Ku Bombay, India, posachedwapa pamene Billy (mnyamata wanga) ndi ine tinali kumeneko pamsonkhano waukulu pamene Ahindu makumi a zikwi anapereka miyoyo yao kwa Khristu, kunadza chenjezo lalikulu. Ndipo ndikufuna inu muone nzeru ya zolengedwa. Ndipo mwadzidzidzi, mosadziwika chifukwa chake, mbalame zazing’ono zonse mu mzindawo zinayamba kuchoka kupita kuthengo. Ndipo mbalame mwaunyanji, zinayamba kupita kuthengo. Ndipo anayamba kuona ziweto zonse ndi nkhoa ndi ng’ombe. Koma ku India, mipanda yawo siili monga mipanda yathuyi, si mipanda ya matabwa, ndi mipanda ya miyala yaikulu yomangidwa yaitali. Ndipo ziweto zonse zinayamba kuchoka ku makoma amenewo, ndi kuchoka ku makhola amenewo, nizipita mpaka pakati pa dambo niziyaamba kuunjikana pamodzi pakati pa dambolo. Ndiye, Mwadzidzidzi chivomezi chachikulu chinagwedeza ndi kugwetsa makoma, mitengo, miyala, zokhoza kuvulaza zinkangouluka. Ndipo mbalame sizinabwerere, nazo ziweto zinangokhala kudambo komweko, ndipo anthu ankangoyenda akuganiza kuti zathano. Ndipo tsiku linalo, chivomezi china chinagwedeza, ndipo nyumba zambiri zinagwa ndi zibuluma zikungouluka. Ndipo pa tsiku lachitatu lakelo, ziweto zinabwerera ku makoma ndi mbalame zinabwerera ku mzinda.

³⁶ O, Iye amene amadyetsa mpheta, Iye amene anadzetsa tolengedwa Take tonse kuti tilowe mu chombo, ali ndi moyobe ndipo akulamulira. Ndipo izo zikuoneka ngati ziri ndi nzeru zambiri pa zochita za Mulungu, kusiyana ndi momwe munthu achitira, amene analengedwa ndi Iye mwa chifaniziro Chake; pamene, munthu amachita mwano. Zolengedwa zazing’ono za pa dziko lapansi, Mulungu amazisamalira ndipo zinachoka ku makoma akuluwo. Bwenzi zitaphedwa,

mbalame zikanangoperedwa m'ming'alu ya matanthwe pamene ankagwedezekera uku ndi uko.

³⁷ Zizindikiro za Kudza Kwake! O, ndi tsiku lopambana limene tsopano tikukhalamo. Zivomezi m'malo osiyanasiyana, matenda, zinthu zonsezo zimene Yesu anazinena zafika. Mwa njira yanga ya kuwona izi, ine sindikuona china chimene chatsala koma Kudza Kwa Ambuye. Kwayandikira.

³⁸ Yesu paku... pakulankhula Kwakenso kwa anthu Ake, Iye anati, "Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu. Pamene uli wanthete ndi pamene uyamba kukhala ndi masamba, inu mumati dzinja layandikira. Ndipo pamene mudzaona izi zikuyamba kuchitika, dziwani kuti nthawi yayandikira.

³⁹ Tazindikirani chimene mtengo wa mkuyu unali. Mtengo wa mkuyu nthawi zonse wakhala fuko la Chiyuda. Iye sanati 'Mtengo wa mkuyu' wokha koma "mitengo yinanso". "Pamene mudzaona mtengo wa mkuyu ndi mitengo yinayonse ikuyamba kukhala ndi masamba." Tsopano, Iye sanalankhule za mtengo wa mkuyu wokha, komanso mitengo *yina* yonse.

⁴⁰ Tsopano, tiyeni tingowona pamene ikuyamba kukhala ndi masamba. Ife takhala mu nthawi ya mtundu wina kwambiri mu zaka zingapo zapitazi. Mpingo wa Amitundu walandira chitsitsimutso chachikulu kusiyana ndi zonse zimene zinalipo kale lonse... chithere cha masiku a atumwi; o, ndipo mpingo wa Amitundu unalibenso chitsitsimutso nthawi yonseyi, inali nthawi ya mpingo wa Chiyuda pamene iwo anali ndi chitsitsimutso. Koma mpingo wa Amitundu kwa zaka khumi kapena khumi ndi ziwiri zapitazo, walandira chitsitsimutso chachikulu chimene kunalibe mu mbiriyakale yonse.

⁴¹ Ife tikuganizira za chitsitsimutso cha Marteni Lutera, inde bwana, chinali chopambana, koma icho chinali ku Jeremane kokha. Ie tikuganiza za chitsitsimutso cha Wesile chimene chinali ku Ingalande, chinafalitsikira mpakana kuno, ndi Zirumba zingapo za a Britishi, koma sizinawakhuze anthu kwambiri. Koma m'amasiku ano, chitsitsimutso chimene chiripo ichi, cha Zosachitikawamba, chafalikira mwathunthu kuchokera ku nyanja zazikulu kukafika ku zinzake kwina kutali, mdziko monse, kupyolera ma mawaillesi otchuka ndi magazini ndi alaliki amene anapita kunjira, mosathandizidwa ndi mtundu wa anthu, ndipo chabweretsa chitsitsimutso chimene chadzetsa zikwizikwi (za miyoyo) imene yabadwira ku Ufumu wa Mulungu.

⁴² Mu ka utimiki kanga kosalimbaka kamene Ambuye anandipatsa, ndaona miyoyo yokhoza kupyola milioni ikudza ku Ufumu wa Mulungu. Tangoganizirani pamenepo! Pamene ena ndi mautimiki otchuka, amene akumveka konsekonse pa walesi, ndi zina zotero, afikitsa mamiloni. Pali moto wa chitsitsimutso umene wayatsa phiri lirilonse mdziko monse,

pafupifupidi, kuyambira pamene ine . . . kuyambira pafupifupi zaka khumi zapitazo, kuyambira pamene ine . . . ife tinayamba mu chitsitsimutso. Tiri pa chitsiriziro cha nthawi.

⁴³ Tsopano zindikirani, koteru, zisanachitike zimenezo, Iye ananenera apa nati, “Makoma a Yerusalemu adzaponderezedwa pansu ndi Amitundu mpakana pomwe nthawi ya Amitundu iti idzatsirizidwe.” Anthu a Muhamadi analanda mzindawo. Iye tikuzindikira zimenezo. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muone vuto limene liripo usiku uno, momwe Ishmaele ndi Isake akugwiranirabe pakhosi la wina ndi nzake, ku Yerusalemu komwe ananeneratu kuti iwo adzakakhalako. Ndipo zaka zingapo zapitazo kunali pafupifupi kopanda M’yuda aliyense mu Yerusalemu.

⁴⁴ Tsopano, Yesu akulankhula, “Pamene muona mtengo wa mkuyu ukuyamba masamba.” Tsopano, Ayuda akhala omwazikana ku dziko lonse lapansi, chiwerengero chachikulu, mamilioni ku Jeremane, ndi ku Itale, ndi ku Amerika ndi pa dziko lonse lapansi. Ndipo Mulungu, monga momwe Iye anachitira mmasiku oyamba, anaumitsa mtima wa Farao, Iye analimbitsanso mtima wa Mussolini pa Ayuda, ndipo Ayuda anathamangitsidwa ku Itale. Iye analimbitsa mtima wa Hitila, ndipo iwo anathamangitsidwa ku Jeremane. Iye analimbitsanso mtima wa Stalini, ndipo iwo anathamangitsidwa ku Russia.

⁴⁵ Ndipo kodi mwakhala mukuona mu mapepala, kuti ife, Amerika, tikuyima mbali ya Aluya? O, m’bale, Chilembo cha pakhoma! Mulungu anati, “Aliyense amene adalitsa Israeli adzadalitsidwa, amene atemberera Israeli adzatembereredwa.”

⁴⁶ Tsopano, ine ndiri ndi chithunzi kunyumba kwathu, kapena ndikukhulupirira kuti chabwerekedwa pa nthawi ino, chotchchedwa ndi anthu a sayansi, “Maminiti Atatu Tisanafike Pakati Pa Usiku.” Ngati dziko la sayansi lati, “koloko yazungulira mpaka kuti ili maminiti atatu kuti tifike pakati pa usiku,” ndipo ine ndikuganiza kuti ayichepetsa tsopano mpaka ili pafupi miniti imodzi kuti ifike pakati pa usiku, pamene anatulukira mipweya yotchedwa haidrojeni kapena oxijeni, atomiki, ndi zimphamvu zazikulu zonsezo zimene akukhoza kuzisunga, zikhoza kusungunula chirichonse kwathunthu pa nthawi ya maminiti asanu okha. Iwo akhoza, mwa mtheradi usiku uno, kuchititsa kuti kusakhale ngakhale munthu mmodzi Kumpoto kwa Amerika konse pa maminiti 30. Ndipo zimenezo ziri m’manja a anthu osakhulupirira amene amatida ife. Ndipo, pambali pa zimenezo, tiri ndi zombo ndi masitima okhazikitsidwa, zoyikidwa mozina, konse konse. . . ku Siberia, mpaka ku Hangare ndi malo osiyana, kumene kuli sitima zathu mokonzeka, zopachiridwa mizinga ya mtundu womwewo.

⁴⁷ Abale, nthawi yapita mosiyana ndi momwe inu mukuganizira! Sodomu ndi Gomorrah ankadziwa mochepe,

usiku uja, pamene iwo anali moyo mu ora lawo lotsirizira. Igupto ankadziwanso mochepa za kuti mngelo wa imfa, amene ananeneredweratu za kudza kwake, kuti akanakhoza kudza usiku umenewo. Anthu a ku Pearl Harbour ankadziwa mochepa kuti chiwembu chichitika. Ife tayikidwa pa muyezo ndi kupezedwa operewera! Tayandikira nthawi yotsiriza!

⁴⁸ Chikanachitika ndi chiyani ngati...Iwo, ku Moscow komweko, akanalondolera mizingayo, potsogozedwa ndi nyenyezi ndi zida zaukazitape m'mwamba, akanakhoza kugwetsera bomba mosaphonya pa Msewu Wachinayi ku Louisville ngati atafuna kuteru. Ndi zoonu. Ndipo ife tikhoza kuyima mu nyanja kwina kwake kumeneko, mu masitima athu, ndi kumalondolera molunjikadi mu mzinda waukulu wa Moscow ngati tikufuna kuteru. Chikanachitika ndichiyani m'bale wanga, ngati mzinga waukulu ukanatembenuka nizichitika ndipo dziko ili nilizizimutsidwa, pa nthawi yomweyo ifenso tikanamasula zathu ndi kulakatitsiranso yathu ku mbali yinayo? Ndipo ife tikukhala pa kabanthu kakang'ono ng'ono zedi kopyapayala, momwe zivomezi zadyaidya mbali zonse mpakana kuti dziko langokhala ngati dzira loswedwa likutayikira. Litangoti liphulike kwakukulu kamodzi ndi pamene phala lotentha limene kuchuluka kwake ndi 8,000 mailosi mkatimu likhoza kuferukira m'mwamba, ndi kuchita chomwecho chimene Mulungu anati chidzachitika.

⁴⁹ Ife tiri kunthawi yotsiriza, tafika. Palibe njira yoletsera izi kuti zisachitike. Kupempha konse...Tikhoza kuyika a Izenihawa mu boma lirilonse, ndipo sizingaletse. Yesu Khristu anati nthawi izi zidzafika, tafika basi. Mtengo wa mkuyu wayamba kukhala ndi masamba.

⁵⁰ Mu chithunzi ichi, komwe ku Irani uko, inu mukuziwerenga mu magazine ya '*Look*' momwe iwo anatenga ndege zazikulu nawapachira Ayuda m'menemo. Zikwi za iwo, amene anali kumeneko kuyambira pa nthawi imene anatengedwa mu ukapolo kunka ku Babeloni, akhala ali kumeneko kwa zaka 2500, ndipo anagotsalira komweko. Iwo ankalimira makasu a pamitengo. Iwo sanadziwe kanthu zakuti Yesu anadza pa dziko lapansi. Sanadziwe kanthu za china chirichonse koma khalidwe lawo lakale la Chiyuda, miyambo imene amakhala moyo nayo. Ndipo pamene ndege izi zinatera ndi kuyamba kuwapachira Ayuda awa, kuwabwezeretsa iwo ku dziko la kwawo. . .

⁵¹ Mneneri ananenera zaka 2800 kapena 3000 zapitazo, anati, "Pamene ati azidzatuluka mu nsinga, Mulungu adzadza nawo pa mapiko a mphungu." Mneneri anaona ndege zikudza, iye anawona zikutera, ndi kuwanyamula iwo kubwerera nawo ku dziko la kwawo. Iye sanadziwe kuti azitche chiyani, anango. . . Zinkawoneka ngati mphungu kwa iye, koteru anati, "Iwo adzabwezeretsedwa pa mapiko a mphungu."

⁵² Ndipo pamene anatsika pa zombo za m'mwambazo ndipo ang'ono akumawathandiza akulu, anafunsidwa. Ndipo iwo anati, "Kodi mwabwerera ku dziko la kwanu kudzafa?"

Iwo anati, "Ayi. Tabwerera kudzaona Mesiya!"

⁵³ O, zimasitima zazikulu zochokera kuzungulira dziko lapansi, mu zaka zingapo zotsiriza, zafukizira utsi wawo kunka ku Yerusalemu zitanyamula Ayuda okalamba, aang'ono ndi akulu, atavala mikanjo yawo, akuchokera kummawa, kuchokera kumadzulo. Ndipo mu mzinda waukulu wa Yerusalemu mbendera yakale yokhala ndi nyenyezi ya nsonga 6 ya Davide ili petupetu, mbendera yakale kwambiri pa dziko lonse lapansi, imene sinauluke kwa zaka 2500, yavomerezedwa ngati ya pfuko usiku uno. Mtengo wa mkuyu wayamba kukhala ndi masamba.

Yerusalemu akukula, Ambuye akubwezeretsa,
Zizindikiro zimene aneneri adanenera;
Nthawi ya Amitundu yakwanira, ndi zovuta
zakwanira

Bwerani, omwazika, kwanu.

Pakuti tsiku lachiwombolo lafika

Mitima ya anthu ikulephera mwa mantha

Mudzazidwe ndi Mzimu wa Mulungu, nyali
zikonzedwe niziwale,

Yang'anani mmwamba! Chipulumutso chanu
chayandika.

⁵⁴ Nthawi yapita mosiyana ndi momwe tikuganizira. Sitimadza ku tchalitchi kudzadzazitsa mipando, sitimadza ku tchalitchi kudzamva ulaliki wabwino, kapena kudza ku tchalitchi kudzamva nyimbo zabwino. Zonsezo ziri ndi malo ake, koma chimene ife tiyenera kudzera ku tchalitchi ndi kudzadzifufuza pamaso pa Mulungu ndi za chipulumutso chathu, poona kuti tsiku la chiwombolo lafika.

⁵⁵ Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, anafanizira ichi Iyi anati kwa mkazi. Ndipo mu phunziro lathu usiku uno, tikupeza mkazi uyu, mwamuna wake anali atachoka, ndipo iye anataya chimodzi mwa zigwinjiri za pa chovala pamutu pake. Tsopano ndiyesa kufotokoza zimenezo.

⁵⁶ Lero, ngati mkazi akwatiwa, iye ayenera kuvala mphete ya chikwati monga chisonyezo cha kuti iye ndi wokwatiwa. Uko ndi kuletsa amuna ena kuti asamakhale ndi chochita naye. Iwo amayang'ana ndipo amaona kuti iye ndi wokwatiwa.

⁵⁷ Mu masiku amenewo, analibe mphete za chikwati, anali ndi chovala mophatika (ankachitcha icho "tablet") ankachivala pa mitu yawo. Ichi chinali ndi zigwinjiri khumi, ndipo ankachiphatika pamitu yawo. Ndipo chimenecho chinali chisonyezo chakuti iwo anali akazi okwatiwa, ndipo mwamuna aliyense samayenera kuchita nawo mopusa, anyamata samayenera kuwazunguza iwowa. Iwo anali okwatiwa.

58 Chirichonse cha zigwinjiri zimenezo. . . Ngati tiri ndi nthawi chabe (koma ndiribe, ndiyesa kusunga mawu anga mofupikitsa momwe ndingathere), ndikanakhoza kukuuzani inu chimene chigwinjiri chirichonse chinkatanthawuza. Chinkaikidwa pamene, ndipo chigwinjiri chirichonse chinkatanthawuza khalidwe lina la mkaziyo. Choyamba, chinkatanthauza chikondi chake kwa mwamuna wake. Chachiwiri, linali lumbiro lake la khalidwe lokhala mosadzidetsa kwa mwamunayo. Ndipo chachitatu ndi chachinayi ndi chachisanu, kupitirira mpaka ku chachisanu ndi zinai ndi cha khumi.

59 Ngati mukufuna kuziyang'ana, onani pa Agalatiya 5. Mupeza kuti mkaziyo ankayimira Mpingo, ndipo Mpingo ndiwo Mkazi wotomeredwa ndi Khristu. Ndipo chibadiri chimene Mpingo ukuyenera kuvala chikupezeka pa Agalatiya 5, chimene chiri chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, kukoma mtima, chifatso, chiletso, chipiriro. Icho ndicho chibadiri chimene chiyenera kuvalidwa ndi Mpingo, chikondi cha paabale, chifundo, chiyanjano.

60 Ndipo mkazi uyu, pamene icho. . .Kuyenera kukhala kutayamba kuda pamene anazindikira kuti anagwetsa chimodzi cha zigwinjirizo.

61 O, pakanakhala nthawi yakuti mpingo ulingalire zofufuza ngati uli ndi zigwinjiri zonse pa icho, ikanakhala tsopano lino. Kukuyamba kuda. Zo—zonjenjemeretsa zomwe ndi mitambo yowononga chitukuko zikuyandama pamwamba pa dziko, tchimo ndi ziwerewere konsekonse. Tikukhala mu nthawi yopambana pamene kuli uthakati, anthu kumangopita ku tchalitchi monyengezera chabe, anthu amene akupita ku tchalitchi pofuna kubisa kulimba mtima kwawo, anthu amene amapita ku tchalitchi namadzitcha Akhristu pamene akukhala moyo wofanana ndi anthu onse a mdziko, kumwa mowa, kusuta fodya, juga, akazi ovala mwa dama, kuvala zovala zimene sayenera kuvala mu—mu chipinda chawo chovaliramo, napita kukaoneka nazo kwa anthu onse m'misewu. Ndipo chikondi cha pa abale ndi chinthu chimene changotsala pang'ono kuyiwalika. Sitinataye chigwinjiri *chimodzi* chokha, koma tataya kwenikweni *chirichonse* cha izo.

62 Ndipo kunayamba kuda, ndipo kumbukirani, mwamuna wake anali kudza. Ndipo ngati akanadzamupeza iye wopanda chimodzi cha zigwinjiri, zikanadzasonyeza kuti iye anali atalembedwa “hule.”

63 Ndipo ngati anadetsa, kapena anadzidetsa mwa njira yina iliyonse ndipo zinawonedwa ndi anthu, iwo amadza naye pamaso pa ansembe ndipo amadza ndi mboni zosimikizira kuti anapezedwa motero, ndipo ansembe poona kuti anali mkazi wokwatiwa, amachotsa chigwinjiri (pa chibadiri chakecho) kuti adziwike kuti amachita nacho cholakwa. Ngati iye anali—

anawononga khalidwe lake, amachotsa chigwinjiri chimenecho. Ngati iye amadzifunitsa, kusonyeza kuti sanali woona kwa mwamuna wake, iwo amachotsapo chimodzi. Chirichonse chimene chinali, iwo amachotsa chigwinjiri chake. Ndipo pamene mwamuna wake amadza, iye amapeza mkazi wake ali ndi chizindikiro, ndipo iye amakhoza kuthetsa chikwati nthawi yomweyo ndi kusakhalanso ndi chochita ndi mkazi woteroyo. Iye samafuna mkazi woteroyo.

⁶⁴ Kotero kunali kutayamba kuda pamene mkazi uyu anazindikira kuti anali atataya china chake, inalinsu nthawi ya kudza kwa mwamuna wake, ndipo nthawi imatha.

⁶⁵ Mpingo kuli bwino uzidzifufuza wokha ndi Mawu a Mulungu, ungwiro wathu, kumvera kwathu, kudzipereka kwathu. Tayamba kukhala okwawira mtseri, antola-nkhani, osuta fodya, amiseche, a Yezebeli odzipakapaka penti, chirichonse chimene chiri pa kalendala chimene dziko lonse limachita, mpingo wa Chikhristu ukuyanjanana ndi zinthu zoterozo lero mpakana kuti simungasiyanitse wina kwa mzake. Ndi nthawi yomwe tikanalingalira bwino. Nthawi ikutha.

⁶⁶ Tsopano, pakuti...nthawi imapita mkaziyu anayenera kuyatsa nyale. Ndipo anatenga nyale. Sanangotenga nyale yokha, koma anatenganso tsache napita kukasesa m'nyumbamo.

⁶⁷ O, m'bale! Ngati panali kufunika nthawi ya kuyatsa nyale, kutumiza Kuwala kwa Uthenga konsekonse, Mzimu Woyera kubwerera mu mpingo... Osangoti zongochulukuka za kutengeka, osati zongosangalatsa, osati zongodzichititsa mwa kutengeka, osati zakungolumpha ndi chimwemwe, koma zokuchitikira mkati mwa mtima wako monga mwamuna kapena mkazi amene wakonza moyo wake kwa Mulungu. Chabwino. Ife tiri mu nthawi yotsiriza.

⁶⁸ Ndipo iye anayatsa nyale, kuti imuwunikire. Ndipo m'bale, kanyale kakang'ono kalikonse kamene kali muno kayenera kuyatsidwa usiku uno. Osati chokhacho, koma anatenganso tsache, ndipo a nyumba zoyandikira anaona fumbi likuwuluka. Mkazi uyu anali ndi nthawi yosesa mnyumba kwenikweni, pakuti mwamuna wake anali pafupi kudza. Ndipo ngati akanamugwira iye alibe chigwinjiri chimodzi, akanatchedwa "hule".

⁶⁹ M'bale, ife Mpingo wa Mulungu wamoyo, mu ma ora opambana amene tikukhalamowa, chikutikhuza ife kuti tidzifufuze, kupita pamaso pa Mulungu, kuyatsa nyale ya Mawu a Uthenga, ndi kudziyesa tokha ndi kuona ngati sitiri operewera, kwenikweni pamene tikuwona zinthu zonsezi zikudza. Tiri ku nthawi zotsiriza, Kudza kwa Khristu kwayandikira. Palibe chiyembekezo chinanso mu dziko lonse kwa Mpingo.

⁷⁰ Ndipo onani, mpingo ukungoyenda m'chimbumbuli. Mpingo ulibe chikumbumtimanso. Iwe ukumalephera

kuwadzutsa nkomwe. Baibulo linati iwo adzafika pa khalidwe lotereli pamene akanamadzati, “Taonani, Ambuye athu akuchedwetsa Kudza Kwawo.’ Ndipo azidzadyana nalumana wina ndi mzake, ndi zina zotero, ndi kumenyana.” Lino ndi ora lenilenilo. Zonse zakonzeka. Masamba a bukhu atembenezidwa, momwe zinali motero, ndipo zakonzeka, Kudza kwa Ambuye.

⁷¹ Mpingo wa Lutherani unataya kuwala kwake. Mpingo wa Methodististi unataya kuwala kwake. Mpingo wa Baptististi unataya kuwala kwake. Mpingo wa Chipentekoste unataya kuwala kwake. Kuwala kuli konse kungokhala ngati kunatha.

⁷² Anthu a Chipentekoste, anthu a Holiness, akuchita chimodzimidzi monga a Methodististi. A Methodististi akuchita monga a Baptististi. A Baptististi akuchita monga a Luterani. A Luterani akuchita monga a Katolika. Ndipo zonse zabwerera ku chisakanizikiro chachikulu cha tchimo. Ndi zoonā. Tiri mu nthawi yotsiriza, Kudza kwa Ambuye.

⁷³ Tsopano, mkazi uja anali ndi nthawi yosesa m’nyumba. Iye anakolopa pansi ponse, anasesanso makoma, anachotsa maukonde a akangaude, anapitirizabe mpaka pomwe anapeza chomwe anataya. Ndipo, pamene anatero, anayitana mipingo imzake yina kuti idze tsopano.

⁷⁴ Ine sindikusamala ngati inu muli a Methodististi, Baptististi, Chipentekoste, Chipresibeteria, idzani, tiyeni tisangalale pamodzi. Pamene nthawi imeneyo idza, pamene mpingo uti upeze chikondi chake cha pa abale, pamene mpingo ukapeza khalidwe la chiyero, pamene mpingo uti udzapeze malo ake mwa Khristu, udzayitanira kwa ziwalo zina za thupi kuti, “Idzani nimukondwe nafe.” Mulungu akufuna mpingo uzimukonda Iye.

⁷⁵ Ndikukhulupirira unali m’mawa wa Lamulungu pamene ndinkanena za makhalidwe a mkazi, kudala kwake, ndi ndani amene angapeze chinthu chokoma koposa kudza kunyumba uli wotopa pamene Mulungu wapereka kwa mwamuna mkazi. Mkazi ndi mwamuna sangasiyanitsidwe, iwo ndi m’modzi. Mu chilengedwe, Mulungu anawalenga iwo poyamba mophatikizidwa pamodzi, ndipo iwo ndi a mtima umodzi, moyo, lingaliro ndi zina zonse. Pamene anapanga munthu kuchokera ku fumbi la padziko lapansi, Iye anampatula mkaziyo kuchokera mwa mwamunayo. Pamene Iye anapanga Eva, Iye sanapita kukapanga-mkazi, pakutenga dothi *lina*, koma anachotsa kuchokera mu nthiti ya Adamu napanga mkazi wake. Iye anati, “Uyu ndi fupa la fupa langa, m’nofu wa m’nofu wanga.” Iwo anali mmodzi mwa mtima, moyo ndi thupi.

⁷⁶ Ndi choyimira Khristu. Mulungu sanatenge Mpingo wa Khristu kuchokera pa ndakatulo, sanatengenso Iwo kuchokera mu chipembedzo. Iye anawutenga Iwo kuchokera mu mtima wa Khristu, nthungo mu nthiti Mwake, kupyolera mu Magazi.

⁷⁷ M'bale wanga, mlongo, ine sindikusamala momwe inu mungakhalire wa chipembedzo, ngati simunakutidwe ndi Magazi, mwatayika. Tifika pa chimenecho, usiku wa nkuja, kuwonetsa momwe ziri zofunikira. Koma inu ndi otayika popanda Mwazi.

⁷⁸ Tsopano, ndiye pamene Iye anapanga mkazi uja, anali bwenzi wake. Chinali china chake chakuti iyeyu azichikonda, chinali gawo la iyemwini.

⁷⁹ Tsopano mvetsani mwatcheru. Mwamuna kapena mkazi sangapite Kumwamba pokhapokha atabadwa kachiwiri. Sindikutanthauza chifukwa munalankhula ndi malirime, sindikutanthauza chifukwa munafuula, sindikutanthawuza chifukwa munavina, sindikutanthawuza chifukwa mumapita ku tchalitchi nthawi zonse, kaya mumavala zikwangani za kukhulupirika kwanu; zinthu zonsezo ndi zabwino, koma Izo sizimenezo. Payenera kukhala kumangirizana kwa chiyanjano chamtheradi pakati pa iwe ndi Khristu, mpaka mutakhala mmodzi. Ndinu mmodzi! Ndipo ngati simuli choncho, bwanji. . .

⁸⁰ Kodi mungalingalire kubwera nthawi ya usiku, wotopa, wofooka, olema? Ngati muli mlimi, makaniko, mlaliki, chirichonse chomwe muli, kubwera, pamene mukupita kukanyumba kanu, mumafuna kuti mukafikeko. Mutatsegula pakhomo ndipo kamkazi kanu kachikondi katayima pamene, nakuchingamirani. M'menemo atasambasamba zonse ziri mwa ukhondo. Nayenda kudza kwa inu nadzakupsyopsonani pa tsaya, nati "Adadi mwatopa." Nakukhazikani mu mpando, iye nadzikhazika m'mikono yanu, nakuyangatani ndi mikono yake namakusisitani. Umangokhala ngati siunatopenso, chimakhala chokupatsa mphamvu. Ndi chinthu china chimene Mulungu anakupatsani ndi cholinga chimenecho. Ilo ndi gawo lanu lomwe, tsopano, ngati ali mkazi woota.

⁸¹ Koma bwanji ngati milomo imeneyo amapsyopsonera mwamuna wina tsiku limenero kapena nthawi yina? Bwanji ngati iwe ukuzindikira zimenezo? Bwanji ngati manja amenewo amakumbatira mwamuna wina? Mkazi woteroyo ndi temberero mmikono mwako. Kupsyopsona kumeneko kumatentha ngati kupsyopsona kwa Yudas. Mikono imeneyo, ungangofuna bola akanati asakuyangate nayo. O, akhoza kukhala atadzikongoletsa, tsitsi lake atalikonzakonza, maso ake akhoza kukhala a bulauni, masaya ake akhoza kukhala a chikasu, kasiketi kake kakhoza kukhala atakasita, akhoza kukhala wokongola kwambiri, koma ulemu weniweni mwa umulungu ndi chikondi ndi kudalirika palibe, kunali bwino atachoka m'mikono mwako. Siungafune kukhala ndi chochita naye, iye—ndi chodetsa kwa iwe. Ziribe kanthu momwe amadzikongoletsera yekha, ali wolakwabe mpakana pomwe angasimikizike kuti ndi wapamtima weniweni,

wosakonda munthu winanso koma iwe wekha, milomo yake yosapsyopsonedwa ndi ya wina koma ndi yako, palibe mikono yina imene imamuyangata koma yako, ndiponso iweyo ukudziwadi. Ndi zabwino bwanji, ndi zotonthoza bwanji!

⁸² Ameneyo ndi mwamuna ndi mkazi wake, amene ayimira Khristu ndi Mpingo Wake. Ndipo pamene mupita ku mpingo wanu, inu mukhoza kukhala ndi anthu ochuluka koposa mu mzindawo, mukhoza kukhala chitchalitchi choonekera patali mumzinda monsemo, mukhoza kukhala ndi limba lapamwamba, mukhoza kumavala mokongola koposa, mukhoza kumayimba ngati chingolopiyo, koma zonsezo, ngati mukumapsyopsonana ndi kumavulira dziko lapansi, kupsyopsona kumeneko pa masaya a Khristu ndi kwa Uyudasi. Iye safuna kuchita nanu kalikonse. Iye amayang'ana pa mphete ya chitomero ndipo Iye amapeza chigwinjiri chitachotsedwa, Iye amapeza chikondi chachoka. Ndi mawonekedwe, Iye wapeza kukhulupirika kutachoka. Iwe wachita chiwerewere ndi dziko lapansi. Iwe umapita ku zovina ndi maphwando a gwedemula, ndi kumaonera mapologaramu onyansa a pa televizioni. Iwe ukuchita chigololo kwa Khristu, kwa Iye, monga pakumutcha Iye Mwamuna wako.

⁸³ Baibulo linati, "Inu mukuti, 'Ine ndi wolemera, sindisowa kanthu.'" Koma Iye anati, "Siukudziwa kuti ndiwe wa mariseche, womvetsa chisoni, wakhungu, wosauka, ndipo siukudziwa." Ino ndi nthawi imene tiyenera kuyatsa nyale ndi kusesa m'nyumba. Kudza kwa Ambuye kwayandikira.

⁸⁴ Tiyeni tiganizire pamenepa kwa maminiti angapo titaweramitsa mitu yathu. Mungatero? Mungapotolokere ku piano, mlongo?

⁸⁵ Kodi mwakhala mukuchita chiyani, mpingo? Muli motani usiku uno? Pamene manja anu ali okwezedwa mwa kudzipereka kwanu, kodi chiripo chimene chakutsutsani? Ngati mukuvulira dziko lapansi, ngati mukuchita zinthu zimene ziri zolakwa, kupsyopsona kwanu . . .

⁸⁶ Ganiziranipo, bambo. Abwana, ine ndikufuna kukufunsani chinachake. Ndipo ichi ndi chokhudzanso madona, ndi akazi a uje. . . Msungwana, mungaganizire bwanji za bwenzi wanu, ngati mukanadziwa kuti munamuwona iye akupsyopsonana ndiponso kuyenda ndi atsikana ena, koma inu mutatomerana naye, ndipo iye nadzasisita dzanja lanu nati, "Wokonedwa, ndimakonda iwe wekha?"

Inu munganene kuti, "Iwe kamunthu kachinyengo, choka pamaso panga!"

⁸⁷ Mukanatani. . . Tangoganizirani, Abwana. Ife sitinangotomeredwa kokha koma takwatira. Mpingo wakwatiwa ndi Khristu. Ife ndi Mkazi wa Khristu, kumamuberekera ana. Inu mungakonde chotani kufika kunyumba usiku,

mwa kudzipereka kwa mkazi wanu, ndipo mutabereka naye ana ambiri, ndipo mukupeza tsiku limenero...Ndipo pamene akudza kwa inu, o, wapaka penti zikhadabo zake (pamenepo, ngati inu muli achikunja). Inu mukhoza... Akhoza kuoneka mwa kukongola kwake konkuja, koma inu mukudziwa. Tangoganizirani m'bale, ngati mkazi ameneyo amapsyopsonana ndi amuna ena. Ngati mikono imene ikukukumbatirani, namakuuzani kuti amakukondani, koma inu mukudziwa limenero ndi...kuti iye wakonda enanso, chikondi chake sichoona. Chikondi chake sichoona. Sichaiwe wekha, ndi cha kwa enanso. Ngati pali mwamuna wina pambali pa iwe, ukhoza kumukankha achoke m'mikono yako. Tangoganizirani momwe mungamvere. Taganizirani mayi, ngati mwamuna wanu adza kunyumba. Osati chabe kokha, koma atatenga matenda a chiwerewere.

⁸⁸ Ndipo, o, dalitsani mtima wanu, mpingo wangodyekadyeka ndi chindoko chauzimu, cha tiziganizo tosiyana siyana ndi zina zonse. Ndi kulakwa! Mulungu, achite chifundo! Yesu akudza, anzanga. Inu simudzakhalanso ndi nthawi usiku wina, kapena tsiku lina. Muyenera kudzifufuza pakali pano.

Tiyeni tipemphere:

⁸⁹ Ndi angati a inu amene mukuti, "M'bale Branham," mitu yanu mutaiweramitsa, manja anu mutakweza, "ndikumbukireni mu pemphero lanu, M'bale Branham. Ndikudza usiku uno, ine sindinadze kuno kudzalankhula zinthu..."? Mulungu akudalitseni. Tangoonani manjawa. "Ine sindinadze kuno kuti ndidzawonedwe, ndinadza kudzapeza chinachake. Ndipo ndikukhulupirira kuti Mulungu walankhula kwa mtima wanga pamene mumalalikira, ndipo ine ndazindikira kuti ndimalakwa. Ine—ine ndikufuna ndikhale weniweni, Mkhristu woono. Ndikufuna ndikhale wokonda kwenikweni, kuti pamene ndipita kwa Ambuye wanga ndi kugwada pa maondo anga, ine ndikufuna Iye adzandikumbatire ine mmikono Yake, nati, 'O, wondikonda Wanga!'"

⁹⁰ Inu mukukumbukira Solomoni, momwe iye ananenera za ichi? Iye anati, "Idza wokonedwa wanga, tiye tikayende m'mipesa, tiye tikayende mminda ya zonunkhira". Momwe ananenera kuti milomo ya mkazi wake kuti inali yooneka ngati duwa lokongola ndi zina zotero. Momwe ankamukondera mkazi wakeyo, anatinso, "Bwera, tiye tikakwaniritse chikondi chatu."

⁹¹ Pamene mugwada pa guwa lanu nimupemphera, kodi moyo wanu umakhala woonadi ndipo moyo wasokonezeka kuti mumati, "Ambuye Mulungu, tiyeni tipatsane chikondi chatu;" ndi kuti, "Inde, Wondikonda wanga, ine ndimakukondani Inu?" Kapena, kodi mwakhala mukuchita ziwerewere? Kodi mwakhala mukuvula kwa dziko lapansi?

⁹² Ndipo ora la Ambuye layandikira pamene zizindikiro zonsezi ndi zozizwitsa, ndi zikwi makumi za zinthu zina zimene zachitika, kulozera, chichiri chirichonse chikulozera. Kwayamba kuda. Mu mpingo mwafika chizizira. Chitsitsimutso chikukhala ngati chatha. Kachigawo kake kotsirizira kangotha kumene. Ndi pomweno pano tikudzipeza tiri mu chogololo. Nanga Iye adzatani? Iye adzaticankha ife kuti tichoke m'mikono Yake, nati, "Choka kwa Ine, iwe wakuchita kusaweruzika."

⁹³ Tsopano, ngati pali wina pano akufuna kukumbukiridwanso, ndikhoza kufunsa pa miniti ino, akweze manja ake kwa Mulungu, kunena, "Ndikudzipezeka tsopano ndi kunena, mwa chisomo cha Mulungu, kuyambira usiku uno ndidzakhala moyo wona mwa kuthandizidwa ndi Mulungu." Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni. Ndi inu m'bale, inu mlongo, inu msungwana, inu bwana, inu m'bale, inu muli apa, pansi apa, ndi inu mnyamata.

⁹⁴ Pali munthu pano woti sanapulumsidwe, anganene, "M'bale Branham, mundikumbukire, ine sindinabadwensu kachiwiri. Ndikudziwa sindinatero?" Mverani, inu ndi osapulumsidwa mpaka mutabadwansu kachiwiri, inu munangotembuzira nkhope yanu kuloza ku Chinachake; koma pamene muvomereza Khristu muli obdwansu kachiwiri. Mukuti, "M'bale Branham, Ine sindinachilandire ai. Ndikudziwa ndiri wolakwa. Ine tsopano ndakweza manja anga, ndi kuti, 'Mundikumbukire inenso.' Sindinapulumsidwepo. Sindina—sindinayesere ndikumutumikira Khristu komwe, koma ndikufuna kuyesa kuteru. Mundipempherere, M'bale Branham." Mungatukule dzanja lanu, winawake muno tsopano? Kodi pali munthu mmodzi muno woti sanakhalepo Mkhristu, akadakonda atatukula dzanja lake, kunena "Kumbukirani ine m'bale, mu pemphero?" Mulungu akudalitseni inu, mwana wamwamuna. Wina wakenso anganene, "Kumbukirani ine m'bale?" Mulungu akudalitseni, dona. Wina wakenso, "Kumbukirani ine m'bale, ndikufuna tsopano kukhulupirira pa Ambuye Yesu ndi kuwalandira ngati Mpulumutsi wanga?" Mulungu akudalitseni, m'bale. Choncho ndiye bwino.

⁹⁵ Winawake amanditsutsa tsiku lina, kumati, "M'bale Branham, chifukwa chiani inu mumanena, 'Tukulani dzanja Lanu?'" Mvetsani, palibe wina amakhulupirira kuitanira kuguwa tsopanonso kuposa umo ndichitira. Ine ndimakhulupirira kudza ku guwa, izo ndi zabwino, koma zimenezo sizingakupulumutseni. Ndi malingaliro anu, kusankha kwanu kwa Khristu. Inu mukuti, "Inde, ngati ine ndikanapita ku guwa." Izo ndi zabwino. Koma abale, kodi munalingalirapo pamene mutukula dzanja lanu kuti mumatsutsana ndi lamulo la sayansi lililonse? Dzanja lanu, mwa chilengedwe, mwa mphamvu ya galavite, liyenera kuloza pansi. Ngati mutukula dzanja lanu zimaonetsa kuti pali mphamvu yoposa

chilengedwe mwa inu, imene ili yotheka kutsutsana ndi malamulo a chilengedwe, ndi kutukulira dzanja lanu kuloza kwa Mlengi wanu, China chake mu mtima mwanu chapanga lingaliro. Mulungu amawona inu mukutukula manja anu chimodzimidzi mmene Iye amaonera inu muli pa guwa. Izi, ndizoonna kwenikweni. Ngati muchita motsimikiza, Mulungu amatanthawuza zomwezonso. Koma taonani, abwenzi, inu simungakhale pakati ndi pakati, muyenera kuchita icho motsimikiza.

Tsopano tiyeni tipemphere:

⁹⁶ Atate Akumwamba wa madalitso, usiku uno pachiyambi pa chitsitsimitso ichi, mmene nthawi yathu yatha tsopano, ndi kupitirira pang'ono, ndikupemphani Inu muwamvere chifundo anthu awa. Ndipo perekani, Mulungu Wamphamvu zonse, kuti...Pano usiku uno pafupifupi manja makumi awiri anakwezedwa mu chinyumba chino, kuti iwo akusowa Khristu. O, Mulungu, ndi miyoyo yawo. Mzimu, Mafuta, atsala pang'ono kuthamo. Sipadzakhalanso ena owonjezerapo. Pamene dontho lotsiriza latha mumbiya, kapena muchotengera, sipadzakhalanso Mafuta ena oika mu nyali. Anthu azindikira kuti akukhala mu masiku a kumapeto. Palibenso chiyembekezo pa dziko lapansi kwa ife kunja kwa Khristu. Ndikupempha usiku uno, Ambuye, kuti mwina mwake, mu chisisira cha nyengo ino, mwa kachetechete, kuti Inu tsopano mutumize Mzimu Woyera amene anawachititsa kuti atukule manja awo, ndipo pulumutsani iwo kuchoka ku moyo wa tchimo. Perekani ichi, Atate.

⁹⁷ Ndipo kukhale kuti usanathe msonkhanowu, pakhale ndithu makumi a iwo, ambiri akufuwula ndi Mzimu Woyera. Lolani malo ochitira ubatizo awa, pakhale wina ali pambuyo pa mzake akubatizidwa mu Dzina la mtengo wapatali la Ambuye wathu Yesu Khristu, mmawa Wachiukitsiro, awuke ndi moyo watsopano. O, Atate Wodala Wamuyaya, ndikupemphani kuti Inu muwadalitse iwo. Perekani ichi, Ambuye. Ndipo tsopano, pa nyengo yomwe ino, lolani kusankha kwao kukhale kowona, lolani akulandireni pamene iwo akhalapo. Magome athu ndi pozungulira ponse padzaza ndi anthu, ndipo ndikupempha kuti Inu muwalole anthu awa usiku uno kuti akhale atumiki Anu. Mu Dzina la Khristu.

⁹⁸ Pamene mitu yathu ili yoweramitsidwa, ndikufuna kukufunsani funso lakachetechete. Inu amene munakweza dzanja lanu ndipo mumapemphera, ine ndikudziwa kuti simunatukule dzanja lanu pongofuna kukweza. Munalikweza chifukwa Chinachake chinakuuzani kuti mutero. Ndipo inu mukuti, ndi dzanja liri lokwezedwa, "M'bale Branham, Ine ndikukhulupirira, pamaso pa Mulungu ndi khamu ili lonse, ine ndikukhulupirira kuti kena kake kachitika mu mtima mwanga usiku uno, kuti kuyambira usiku uno kufikira mtsogolo ine

ndikhala munthu wosinthika.” Mungatukule dzanja lanu, inu amene munatukula dzanja, ndi kuti, “Ine ndikukhulupirira?” Mulungu akudalitseni, dona. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu. Zimenezo ndi zopambana. Kutali kumbuyo uko, inde, Ambuye akudalitseni.

⁹⁹ Wina wakenso angatukule dzanja lake, kunena, “Ine ndikukhulupirira tsopano lino?” Mulungu akudalitseni, m’bale. “Ambuye akundiiza usiku uno. . .” Mulungu akudalitseni, mlongo cha kumbuyoko. Mulungu akudalitseni inu, msungwana cha kuno. “Ambuye akundiiza tsopano lino kuti chinachake chachitika mu mtima mwanga, ndipo ndikukhulupirira kuti ndikhala ndi chimwemwe chochuluka mu chitsitsimutso chino kupambana chomwe ndinakhala nacho mmoyo wanga.” Mulungu akudalitseni. Chabwino, Mulungu akudalitseni, dona mwakhala apa. Ndimaganiza ndi nthawi yabwino yoti inu mutukule dzanja lanunso. Pali ena, akunena, “Ine ndikumva kutsinthika, M’bale Branham, Ine ndikhulupirira ndituluka mu tchalitchi usiku uno ndi chikumbumtima cha kudza msanga kwa Khristu. Ine ndituluka muno kukakhala moyo wosinthika. Ine ndikukakhala Mkhristu, mwa chisomo cha Mulungu. Ndikukhulupirira kuti Mulungu wandiitana ine.”

¹⁰⁰ Ndipo ngati Iye wakuyitanani, ndinu Wake. Lekani kudziyalutsa, lekani kudziyalutsa kwa dziko! Tiyeni, khalani moyo ndi lye tsopano. Nenani, “Ndilapa machimo anga onse, ndipo tsopano ndikumutenga Khristu ngati Mpulumutsi wanga.” Pangakhale wina tisanatseke? Alipo kodi? Mulungu akudalitseni, m’bale. Mulungu akudalitseni. Ndi bwino kuteru. Mulungu akudalitseni. Ndi bwino kuteru. Ndikukondwa koposa kuona inu mukuchita zimenezo. Chabwino.

¹⁰¹ Chiyambi cha usiku tsopano, zakhala pang’ono. . . sitifuna kuyika kupsyinya koposa apa, tikufuna kutuluka mofulumira kuti mukhoze kubweranso mawa usiku.

¹⁰² Tisanatseke, pali munthu wodwala amene angatukule dzanja lake, ndi kuti, “Pempherani ine, M’bale Branham?” Chabwino, ndi asanu, asanu ndi limodzi, asanu ndi awiri, asanu ndi atatu, asanu ndi anayi, manja khumi, khumi ndi limodzi, khumi ndi awiri, chabwino, tsopano khumi ndi atatu, khumi ndi anai, chabwino, khumi ndi asanu.

Tiyeni tiwerame tsopano:

¹⁰³ Atate Akumwamba a madalitso, Inu mwaona manja amenewo. Ndipo, o, iwo ali pano ndi cholinga. Mwina mwake iwo ndi Akhristu, koma akusowa chithandizo Chanu chopambana. Ndipo ife tikuzindikira, Ambuye, kuti Inu munafuula kupyolera mwa Davide, kuti “Musayiwale zokoma Zake zonsezi: Amene akhulukira mphulupulu zathu zonse, Amene achiritsa nthenda zathu zonse.” Ndikupemphera kuti Mwazi wa Khristu utera mwa mtengo wapatali pa iwo ndipo achira, kuti udzawakomere

msonkhano uli nkudzawu. Perekani ichi, Ambuye. Kupyolera mu Dzina la Khristu tifunsa ichi. Amen.

¹⁰⁴ Tiyeni tiyimirire tsopano, *“Tenga Dzina la Yesu Nawe.”*

O, Dzinalo la Yesu nawe,
Mwana. . . (Tiyeni titembenuke, kugwirana
chanza ndi wina ali pafupi ndi inu.
Tembenukirani pozungulira, gwiranani
chanza)

Lidzakupatsa chimwemwe ndi chitonthozo,
Tsopano tenga Ilo kulikonse upita.

Dzina lopambana (Dzina lopambana) O,
lokoma

Chiyembekezero cha dziko ndi chimwemwe
cha Kuwamba;

Dzina lopambana (Dzina lopambana), O,
lokoma!

Chiyembekezero cha dziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

¹⁰⁵ Tsopano tiyeni mwakachetechete, mmene tikuyang’ana mbali iyi, tiyimbe mosafuula:

Pa Dzina la Yesu tigwada,
Kugwa pansu pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
korona,
O, pamene ulendo wathu udzatha.

Dzina lopambana (lidalitseni Ho), O, lokoma!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;

Dzina lopambana (Dzina lopambana). O,
lokoma!

Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha
Kumwamba.

¹⁰⁶ Tsopano yangopyola pang’ono 9 koloko, pafupifupi maminiti 7 kapena 8 kupitirira 9 koloko. Mofulumira, mukhoza kukafika kunyumba, kabwereninsu mawa usiku ndipo tidzasangalala ndi madalitso a Mulungu, kumva bwino pokhala nafe. Ndipo tsopano ndinawona pafupifupi manja khumi ndi awiri, khumi ndi anayi atakwezedwa kufuna machiritso usiku uno. Ngati zipitirira mpaka kukhala odwala ochuluka muno, tidzayitanira usiku wa msonkhano wamachiritso, mwina Loweruka usiku ndiponso Lamulungu. Ngati tiwona kuti sitingathe kuwatenga onse Lamulungu, tidzawatenga Loweruka usiku. Tidzawona mmene ziti zidzakhali.

¹⁰⁷ Tsopano Ine—Ine ndipemphera kuti madalitso a Mulungu akhale mozama pa yense wa inu, ndipo Iye akhale ndi inu ndipo adalitse inu mpaka tidzathe kukumananso mawa usiku.

¹⁰⁸ Tiyeni tiweramise mitu yathu mwa kamphindi kapemphero, pamene ndikufunsa abusa kuti abwere kuno nadzatibalalitsa ndi mawu a pemphero.



KUDZA KWACHIWIRI KWA AMBUYE CHA57-0417
(The Second Coming Of The Lord)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu usiku, Epulo 17, 1957, ku Branham Tabernacle, mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1991 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org